Wakhate Anachiritsidwa

Malangizo: Chitani zotsatirazi muli pamalo opanda phokoso. Pamene mukuwerenga mavesiwo, yerekezani kuti inuyo muli nawo pamalopo. Yesani kuona m'maganizo mwanu zimene zikuchitika. Mukhale ngati mukumva zimene anthuwo akulankhula. Yesani kumva mmene anthu a mu nkhaniyi akumvera mu mtima mwawo.

Amene akutchulidwa kwambiri m'nkhaniyi: Namani, Elisa ndi kamtsikana kachiisiraeli kamene sikanatchulidwe dzina

Chidule cha Nkhaniyi: Namani yemwe anali mkulu wa gulu la asilikali a Siriya anachiritsidwa matenda oopsa kamtsikana kena kachiisiraeli katamuuza kuti apite kwa Elisa.

❶ ***ONANI NKHANIYI BWINOBWINO.—WERENGANI 2 MAFUMU 5:1-19.***

Kodi kamtsikana kachiisiraeli kameneka kankamva bwanji katasiyana ndi makolo ake amene anali oopa Mulungu? _____

_____

_____

Kodi mukuganiza kuti Namani yemwe ankadwala matenda oopsa anakhumudwa ndi chiyani? _____

_____

Kodi mukuganiza kuti zinthu zinali bwanji, pamene Namani ankakambirana ndi atumiki ake pa vesi 11 mpaka 13? _____

_____

Kodi Namani anasintha motani mukaona zimene zikunenedwa kuyambira vesi 15? _____

_____

❷ ***FUFUZANI MOZAMA.***

Kodi n'chiyani chinachititsa kuti Namani akhale wodzikuza? (*Werenganinso vesi 1.*) _____

_____

Pogwiritsira ntchito mabuku amene muli nawo, fufuzani za matenda a khate m'nthawi zakale.* (Mwachitsanzo, kodi matenda a khate anali oopsa motani? Kodi anali opatsirana? Kodi ankachiritsidwa bwanji?) _____

_____

_____

_____

* Khate lapakhungu lakale limeneli likuphatikizapo khate lamasiku ano.

Kodi mukuganiza kuti kuchiritsidwa kwa Namani kunakhudza motani kamtsikana kachiisiraeli kaja? _____

Kodi zimene Elisa ananena zinayesa motani Namani? (Onani vesi 10.) _____

❸ ***GWIRITSANI NTCHITO ZIMENE MWAPHUNZIRA. LEMBANI ZIMENE MWAPHUNZIRA ZOKHUDZA . . .***

Kuipa kodzikuza. _____

Kulankhula molimba mtima za chikhulupiriro chanu. _____

Mphamvu za Yehova zochiritsira matenda. _____

❹ ***M'NKHANIYI, KODI NDI MFUNDO ITI IMENE YAKUKHUDZANI MTIMA KWAMBIRI, NDIPO N'CHIFUKWA CHIYANI?***

www.jw.org © 2010 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania